# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE, MAGETSI NDI MIGODI

## NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## NYENGO MSABATAYI


## KUYAMBIRA PA 05 JANUARY, 2025 MPAKA PA 11 JANUARY, 2026

### NYENGO M'SABATA IKUBWERAYI

Kuyambira pa 05 January kufikira lachiwiri pa 06 January 2026, **tiyembekezere nyengo ya mitambo ndiya mvula ya mabingu yomwe izigwa yamphamvu m'madera ena**. **Mvula yamphamvu ikuyembekezereka kuzafalikira m'madera ochulukirapo, makamaka a mphepete mwa nyanja ndi ena a m'chigawo chakum'mwera, kuyambira lachitatu pa 07 January 2026 kufikira lachisanu pa 09 January 2026** ndipo idzachepa mphamvu kuchokera loweruka pa 10 January 2026. Izi ndikamba ka dera lodzetsa mvula lotchedwa ITCZ mothandiza ndi dera la mpweya opepuka lomwe likhale mu Mozambique Channel.

**Chiopsezo cha madzi osefukila ndi chachikulu makamaka ku Salima, Mangochi ndi Nkhotakota.**


**Mphepo iziomba kuchokera mbali zosiyanasiya ndipo iziomba mwamphamvu m'madera omwe mukugwa mvula.**




*Ulosi wamvula musabata ikudzayi. Kuphatikiza masiku onse musabatayi. Mvula ypchuluka ikuyembekezeka ku Salima, Mangichi and Nkhotakota*

### NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI

Kunali nyengo yamitambo ndi ya mvula yamabingu yomwe inagwa yamphamvu m'madera ambiri a mphepete mwa nyanja ndi madera ena a'mchigawo chapakati, makamaka ku Nkhotakota. Mlingo wa mvula yambiri omwe tinalandira unachokera kwa Nkhunga m'boma la Nkhotakota ndi mlingo wa **285.3mm** pa **30 December 2025 omwe ndiopitirira mlingo wokhazikika (average) mu mwezi wa December**. Komanso mvula yonse ya msabatayi kwa Nkhunga inafika **675.7mm** pamene mvula ya mwezi onse wa December yakwana **1062 mm mdera limeneli**. Zimenezi zapangitsa madzi kusefukira ku Nkhotakota ndi madera ozungulira ngati zomwe zinachitika mu mwezi wa March in 2024.




*Mapu akuonetsa kuchuluka kwa mlingo wa mvula yomwe yagwa ku Nkhotakota mu mwezi wa December 2025*

### MALANGIZO M'SABATALI

- **Tipewe kuoloka madzi omwe asefukira kapena omwe akuthamanga kwambiri komanso tipewe kugwiritsa ntchito nyumba kapena zimbuzi zomwe ndizosalimba ndipo zanyowa ndi mvula.**
- **Mvula yamabingu:** Tikhale m'malo otetezeka

***Kuti mudziwe zambiri funsani kwa:*** *The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services, Ministry of Natural Resources and Climate Change, P. O. Box 1808, Blantyre, Malawi. Tel: (265) 882 266 579; Email: metdept@metmalawi.gov.mw , Website: www.metmalawi.gov.mw*

**Malo osindikizira: Blantyre** **Yatulutsidwa Lamulungu pa 04 January, 2026.**